# LANDIRANI YESU

## LOWANI MU UFUMU WA KUMWAMBA

### (Mapemphero a machiritso ndi Magazi a Yesu)

Takulandirani ku ufumu wa kumwamba kudzera mwa Yesu Khristu wa ku Nazareti, Mulungu wamoyo. Yesu Khristu ndiye Njira yokhayo ndi choonadi chokhacho chimene chidzatsogolera Munthu kupita kumwamba **(Yohane 14:6).** Lekani kuchimwa,Lalandirani Yesu lero kuti mukalowe mu ufumu wa kumwamba M'chiweluzo chomaliza chisanafike.

Tinaomboledwa pa mtengo waukulu pa kalvare, ndipo kudzera mwa Yesu Khristu tinapatsidwanso mphamvu, chilimbikitso ndi ulamuliro kudzera Mu mphavu ya mtanda ndi mwazi wa Yesu umene anakhetsa pa kalvare
**(1 akolinto 6:19-20).**

Mwazi wa Yesu watipatsa mphamvu yopambana nkhondo za uzimu ndi Kutimasula ku chipsinjo cha satana. Ndipo pano Satana alibenso mphamvu kapena Ulamuliro pa ife, tinapatsidwa ulamuliro womugonjetsa kudzera mu mwazi wa Ambuye wathu Ndi mpulumutsi Yesu Khristu ( mwazi wa mwana wa khosa ), **chivumbulutso 12:11.** Perekani moyo wanu kwa Yesu Khristu ndi kulowa mu ufumu wa kumwamba, sakhani kuwala, Ndi kuvomeleza kukhala moyo woyera. Yesu ndi njira yokhayo, palibe amene azalowe mu ufumu Wakumwamba ngati salandira Yesu kukhala mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wake.

Ndikukudalitsani mu dzina la Yesu Khristu, amene ali mbuye ndi mpulumutsi wa miyoyo yathu, **Amen.**

**Mulungu akudalitseni,**
**Petrida karch.**

# ZAMKATIMU

Ufumu wa kumwamba pa Dziko lapansi…………………4

Pemphero loti umulandire Yesu…………………..……..6

Malamulo a ufumu wa kumwamba……………………..…..7

Ubwino wakupulumutsidwa/ kulandira Yesu……..…..8

Pangano la mwazi wa Yesu ndi Mphamvu
ya mtanda kwa anthu………………………………………...11

Mphamvu ya Mwazi wa Yesu kwa anthu………………...13

Mphamvu ya Mtanda wa Yesu kwa anthu………..……14

Mapemphero omasuka kuzomangira
Zosiyanasiyana ndi matenda…………..........……………..15

Uthenga wanga kwa inu……………………………………..19

## UFUMU WA KUMWAMBA

## PA DZIKO LA PANSI NDI YESU KHRISTU

Dziko ili linalengedwa kuti likhale kupitiliza kwa ufumu wa kumwamba koma mu thupi. Mulungu ndi mawu, kudzera mu mawu ake analenga kumwamba ndi dziko lapansi, ndipo ichi ndi chifukwa chake timazindikira kuti mawu a Mulungu ndi Mulungu mwini. Analenga munthu **( Adamu ndi Hava)** ndi cholinga choti akhale ndi umwini, alamuliro, komanso ayang'anire dziko lapansi kudzera mwa mzimu umene anaika mwa munthu.

**Mateyu 25:34.**

*Pomwepo mfumuyo idzanena kwa iwo a kudzanja lake lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu ufumu wokonzedwera kwa inu pa chikhazikiro chake cha dziko lapansi.*

**Geneses 1:26-27**

*Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'chifaniziro chathu, monga mwa chikhalidwe chathu: alamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pambalame za m'mlengalenga, ndi pang'ombe, ndi padziko lonse lapansi, ndi pazokwawa zonse zakukwawa padziko lapansi. 27. Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chake, m'chifanizo cha Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi.*

**Masalimo 115: 16**

*Kunena za kumwamba, kumwamba ndiko kwa Yehova; Koma dziko lapansi analipereka kwa ana a anthu.*

Tchimo linampangitsa munthu kutaya mphavu ndi ulamuliro wotenga komanso kulamulira dziko lapansi. Tchimo linapangitsa munthu kutaya ufumu umene anapatsidwa kuti akhalemo ndi mwayi wa Mulungu kukhala mwa iwo ndicholinga choti akhale nawo umwini, ulamuliro ndi

kuyang'anira.Tchimo linapangitsa kusitha kwa ulamuliro pano padziko lapansi ndipo ulamuliro wina watsopano unayambika pano padziko (**ufumu wa satana**). Munthu oyambilira kukhala m'munda wa edeni dziko la uzimu anali ngati mu **ufumu wa kumwamba pa dziko lapansi** ndipo pamene anachita ntchimo lodya chipatso choletsedwa, anapanga tchimo limene linawapangitsa kuti athamangitsidwe kuchoka m'mundawu ( ufumu wa kumwamba) kulowa mu ufumu wa m'dima ( **ufumu wa ziwanda/ sataniki**)

**1 Yohane 3:4**

*Yense wakuchita ntchimo achitanso kusaweluzika; ndipo tchimo ndilo kusaweruzika.*

**Tchimo ndi kuukira** kapena kutsutsana ndi ndondomeko zoyenera. Tchimo limaphwanya **pangano pakati pa Mulungu ndi mtundu wa anthu ( pangano lakutchedwa ana a Mulungu ndi ana a ufumu).**Kulapa/kukhululuka kukhoza kukwanitsa kubwezeletsa ufumu wa kumwamba padziko lapansi ndi ufulu onse umene unalipo pachiyambi kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu,**Chivumbulutso 5:9-10,**

*Ndipo aimba nyimbo yatsopano, ndi kunena, muyenera kulandira bukulo, ndi kulimasula zizindikiro zake; chifukwa mwaphedwa, ndipo mwagulira Mulungu ndi mwazi wanu anthu a mafuko onse, ndi manenedwe onse, ndi mitundu yonse, ndipo udawayesa iwo ufumu ndi ansembe kwa Mulungu wathu; ndipo achita ufumu padziko.*

Ufumu wa kumwamba wabweleranso padziko lapansi kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu monga mfumu yathu yokhala **kumwamba kwa Mulungu**. Njira yokhayo yobwezeretsera ufumu umenewu ndi **kulapa ( kukhululukidwa ndi chipulumutso**),**Mateyu 4:17;**

*Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kulalikira, ndi kunena, Tembenukani mitima, pakuti ufumu wa kumwamba wayandikira*

## PEMPHERO
## LOLANDIRA YESU M'MOYO WANU

Tate mu dzina la Yesu Khristu wa ku Nazareti amene muli ndi moyo. Ambuye Yesu, ndikupepha chikhululuko pa machismo anga onse amene ndakhala ndikuchita kuchokera ku mwana wanga kufikila pano. Chonde chotsani dzina langa mu buku la **gahena** ndi **imfa** ndipo mulilembe mu buku la **moyo wosatha.**Ndikumumukana satana, amithenga ake ndi mizimu yonse yoipa. Ndikuvomeleza inu Yesu Khristu wa ku Nazareti ndipo ndikukulandirani Yesu kuyambira pano kukhala mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wanga onse ndi mzimu wanga kuyambira pano mpaka kalekale.Zikomo, Ambuye yesu, pondiombola ine, kundikhululukira machimo anga ndi kundimasula,**Amen.**

Ngati mwapephera pepheroli ndi chikhulupiliro, zindikilani kuti mwapulumutsidwa ndipo Yesu Khristu akhala mwa inu **( mu ntima mwanu ).** Mwapanga chisakho chabwino cha pano komanso m'tsogolo la moyo wanu. Pakulandira Yesu Khristu, mwaumba ubale wabwino pakati pa inu ndi Yesu Khristu komanso Mulungu wakumwamba chifukwa ndipephero limeneli mwalandira komanso kuvomereza zinthu zitatu izi:

1. **Yesu Khristu**
2. **Mzimu woyera**
3. **Moyo wosatha**

Musamusiye Yesu, pitilizani ndi chipulumutso, samalirani chovala chanu cha chiyero. Mpingo wa Ambuye uli pafupi kukwatulidwa.

✞

**MALAMULO A UFUMU WA KUMWAMBA**

Ufumu uli wonse umakhala ndi mfumu, malamulo ndi chitetezo chimene chimatetezera ufumuwo.Mfumu ya ufumu wa kumwamba ndi Yesu khristu, Mulungu wake ndi Mulungu wa moyo **( Mulungu wa kumwamba),** malamulo ake amanyamulidwa ndi buku loyera ndi chitetezo chake chimatetezedwa ndi akhondo amene amatchedwa kuti angelo woyera **(mzimu woyera).** Ufumu umenewu umatsogozedwa mu dziko la uzimu (dziko losaoneka ndi maso a ku thupi).Dziko la uzimuli linagawadwa magulu awili;

1. **Ufumu wa kumwamba (dziko lowara)**
2. **Ufumu wa satana (ufumu wa mdima)**

Ufumu wa kumwamba umayendetsedwa ndi chikhulupiliro ndipo njira yokhayo yolumikizirana pakati pa Mulungu ndi anthu ake ndikudzera mu pemphero, masophenya, maloto, mawu a Mulungu ndi kuitanidwa kuchokera kwa atumiki ake. Moyo wa munthu muli anthu awiri koma thupi limodzi. Anthu awiri amenewa amakhalira limodzi, ndipo azasiyanitsidwa ndi imfa yokha basi. Pali moyo wa uzimu ndi moyo wa ku thupi. Munthu wa kunja ndi thupi lathu lakunjali, ndipo munthu wa mkati ndi mzimu wathu umene uzakhalabe mpaka kalekale. Munthu wamkati mwathu analengedwa mu uzimu. Pamene tidzafe, moyo uzatenga mzimu ndikuchoka mu thupi, ndi kupita ku mwamba kapena kugahena kukakumana ndi chiweluzo chomaliza.

**Geneses 3:19**

*M'thukuta la nkhope yako udzadya chakudya, kufikira kuti m'menemo unatengedwa: chifukwa kuti ndiwe fumbi, ndi kufumbiko udzabwerera.*

Wamkatiyo kukhala mchizolowezi chomawerenga mawu a mulungu, pemphero, kumvera uthenga wa mulungu, kusala ndi kuchita ntchito zabwino **Mateyu 4:4;**
*"koma iye anayakha nati" kwalembedwa munthu sadzakhala ndi mkate wokha, koma ndi mawu onse a mulungu akutuluka mkamwa mwa Mulungu.*

Ufumu wa kumwamba udalira buku lopatulika (mawu a Mulungu). Mawu a Mulungu ndi Mulungu mwini. Mawu a Mulungu ndi chishango pakati pa anthu ake ndi satana. Malamuro a ufumu wa kumwamba ndi abwino ndipo analembedwa mu Torah ndi Moses **(Detronome 5:6-22)**.

## UBWINO WA CHIPULUMUTSO/ KULANDIRA YESU

Anthu ambiri samadziwa ubwino ndi kufunika kolandira Yesu Khristu. Palibe mphindu lalikulu kwambiri pa dziko lapansi loposa kukhala ndi Yesu Khristu ndi kukhala mu ufumu wake lero mpaka kalekale (ufumu wa kumwamba). Yesu Khristu ndi njira kapena khomo lokhalo lokalowera mu ufumu wa kumwamba, **(Yohane 14:6).**Muzalowa mu ufumu wa kumwamba pokhapokha mutalandira Yesu Khristu kukhala mbuye ndi mpulumutsi wa moyo wanu.

## UBWINO WOLANDIRA YESU KHRISTU

1. Dzina lanu limalembedwa mu buku la moyo wosatha kumwamba.
2. Kulibe matenda ku ufumuwu km moyo wosatha.
3. Umalandira moyo wosatha pompopompo ndi m'moyo winawo ikatha imfa ( chikatha chiweluzo).
4. Mukhala mwachoka mu dziko la mdima ndipo mwalowa dziko la kuwala limene limatsogozedwa ndi Yesu Khristu ngati mfumu ndi Mulungu wa moyo ngati Mulungu wa ufumuwu.

5. Mumatetezedwa ndi angelo oyera **( mzimu woyera)** nthawi zonse ku nyanga kapena ufiti ndi mdima **(numeri 23:23)**
6. Machimo anu amakhululukidwa, matembelero amachotsedwa kwa inu ndipo mumakhala ndi moyo ndikulandira madalitso kuchoka kwa Yesu Khristu **(Yesaya 1:18)**.
7. Mumalandira ufulu ndi chitetezo cha ufumu wa kumwamba, moyo wanu umatetezedwa nthawi zonse.
8. Mumalandira mphavu yazimu woyera kudzera mu mchipulumutso.

Ndikufuna ndikulimbikitseni kwambiri, mwasakha njira yabwino, mwasakha madalitso lero ndi tsogolo la moyo wanu. Mwasakha Yesu Khristu ndipo mwamkana satana; mwasakha kupita kumwamba, ndipo mwakana kupita ku gahena **(Chivumbulutso 20:15)**,Ndipo ngati munthu sanapezedwa olembedwa mbuku lamoyo,anaponyedwa Nyanja yamoto .
Chiweruzo chikubwera ,sithani moyo wano ndikubwerera kwa **Yesu Khristu.**Palibe kukhululikidwa machimo opanda **Yesu Khristu,**ndichichifukwa chake anafere pa mtanda kufuna kupulumusa mitundu yonse ya athu ku kuchiwerudzo chomaliza.kukwatulidwa kwa mpingo kwayandikila,siyani kukhalala moyo wa uchimo,thawilani kwa Yesu ndipo iye azakupulumusani **(kukuimililani)** pa chiweruzo chomaliza chili kudza.Mpingo wake woyera wasala pang'ongo kukwatulidwa,lapani machio anu sopano ndikuzikozekeresa ku mkwaturo wa ambuye. Lowani mu umfumu wa ambuye usanachosedwe padziko la pansi pano.

## CHINA CHITIKA NDICHIYANI MOYO WANU MUTANGOLANDILA YESU KHRISTUS ?

**1).**Mwakhululukidwa machimo anu onse **( 1 Yohane 1:9 )**

**2).**Dzina lanu linalembedwa m'buku la moyo wosatha Kumwamba **(Luka 10:20).**

**3).**Mumakhala wolengedwa watsopano **(2 Akorinto 5:17 ndi Aefeso 4:22-24)**

**4).**Mumatetezedwa ndi angelo oyera nthawi zonse **(Masalimo 91:11-12).**

**5).**Mumakhala likulu la Khristu ndi Mulungu pa dziko lapansi **(Yohane 14:23 ndi Aefeso 2:22).**

**6).**Munalandira ulamuliro pa mdierekezi ndi atumiki ake ndipo ntchito zawo ziribe mphamvu pa inu **(Luka 10:19 ndi Yakobo 4:7).**

**7).**Mudzaukitsidwa ndi kukwatulidwa ndi Yesu akadzabwera kudzatenga mpingo (opulumutsidwa) chifukwa muli ndi moyo wosatha**, ( 1 Atesalonika 4:16-17 ndi Yoh 5:12).**

**8).**Mzimu Woyera amakhala mwa inu **( 1 Akorinto 6:19 ).**

Pamene munalandila Yesu moyo wanu, munakhalaso munthu watsopano,umayamba ulendo watsopano komanso ubale ndi Ambuye Yesu. Osaphwanya ubwenzi ndi Ambuye Yesu,pokhala moyo wachiyero**(wangwiro**)**.**Kanani moyo wauchimo ndipo musabwerereretso ku uchimo**.** Samalilani nkanjo wanu wachiyero ndicholinga choti muzakhale nawo mu gulu lokwatulidwa**.**

✞

**PANGANO LA MWAZI WA YESU**
**NDI MPHAMVU YA MTANDA KWA ANTHU**



Mwazi wa Yesu uli ndi pangano la anthu, uli ndi mphamvu zogonjetsa mdierekezi ndi ufumu wake makamaka masiku otsiriza ano kusanachitike mkwatulo **(Chibvumbulutso 12:11).**Tinagulidwa ndi Mwazi wamtengo wapatali wa Mpulumutsi wathu Yesu Khristu waku Nazarete tamasulidwa ndipo sitilinso akapolo a uchimo, **(1 Akorinto 6:19-20).**Kuyambira tsopano mdierekezi alibenso mphamvu pa ife tapatsidwa mphamvu ndi ulamuliro kudzera mwa Khristu Yesu (Mphamvu ya Mtanda ndi Mwazi wa Mpulumutsi wathu Yesu Khristu) zokhetsedwa pa Kalvare kuti tipambane pankhondoyo ndi kutimasula ife, kutali ndi zowawa ndi ukapolo wa mdierekezi.Tikukhala mu nthawi yotsiriza, pamene tikukonzekera mkwatulo wa mpingo (kubweranso kwa Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu wa ku Nazareti). Nthawi imeneyi si yophweka kwa dziko chifukwa cha nkhondo yachikhulupiriro imene imalepheretsa anthu ambiri kulowa mu Ufumu wa Kumwamba n’kukathera kumoto. Dzina la Yesu, Mzimu Woyera, Mau a Mulungu ndi Mphamvu ya Mtanda zonse ndi zamphamvu koma Mwazi wa Yesu ndi wamphamvu kwambiri mu nthawi ino yokonzekera mkwatulo wa mpingo. Chibvumbulutso cha Yohane ndi buku lomwe limafotokoza za nthawi yotsiriza ya dziko yomwe tikukumana nayo mkwatulo usanachitike.Ufumu wa mdima umagwiritsa ntchito mphamvu zambiri kuti alepheretse anthu ambiri kubwerera kwa Mulungu wamoyo, na kushindwa pokea chipulumutso.

Tikudutsa mu nkhondo yauzimu, yomwe sitingathe kuyipambana ndi mphamvu zaumunthu, koma kudzera mu Mphamvu ya Mzimu Woyera ndi Magazi a Yesu, amene wachita pangano nafe, makamaka m'masiku otsiriza ano **Chivumbulutso 12:11.**

*"Ndipo iwo anamugonjetsa ndi Magazi a Mwanawankhosa ndi mawu a umboni wawo, amene sanakonde moyo wawo ngakhale kufa."*

## MALO 6 AKUCHOKERA MWAZI WA YESU

**1.Mwazi pankhope -** Pamene Yesu anapemphera pa phiri la Getsemane **Luka 22:41 - 44,** madontho a Magazi ochokera pankhope pake anapatsa anthu onse Chisomo cha nkhope, nyenyezi, ndi kutimasula ku zomangira zonse zimene Mdyerekezi **(Satana)** anatimanga.

**2.Mwazi Pamsana -** Pamene Yesu analasidwa pamsana, mwazi umenewu unagwiritsidwa ntchito ngati mankhwala ndi kutimasula ku matenda onse.

**3.Mwazi m'manja –** Pamene Yesu analasidwa m'manja ndi misomali, mwazi wake unatipatsa mphamvu yochiritsa, kuika manja pa odwala ndi kulandira machiritso. Tinalandira ulamuliro wochiritsa matenda onse, **Marko 16:17-18.**

**4.Mwazi wamapazi -** Mwazi wa Yesu umene unakhetsedwa pamapazi atakhomeredwa ndi misomali unatipatsa ufulu wokhala,kugonjetsa mphamvu zonse za mdani,**Salmo 91:13; Luka 10:19; Salmo 60:12.**

**5.Mwazi Pamutu –** Pamene Yesu anavekedwa korona wa minga, Mwazi wake unatsuka matemberero onse amene ife anthu tinatembereredwa nawo kupyola pa dziko lapansi ndi mdierekezi ndipo anatsegula kumvetsa kwathu, nzeru ndi maganizo ndi kutimasula ife, **Genesis 3:17-18 .**

**6.Magazi anatuluka m'mbali –** Magazi a Yesu amene anatuluka m'mbali mwa Yesu pambuyo pa msilikali

kumuwombera Yesu mkuki m'mbali kuti atsimikize kuti wamwalira. Magazi ndi madzi zinatuluka.Anthu tinapeza moyo wosatha kudzera mu Madzi a Moyo, ndipo Magazi ake anatitengera moyo watsopano, powagonjetsa mphamvu za imfa, ndipo anatibwezeretsa ku moyo padziko lapansi. **(Yohane 19:33–34; Masalimo 118:17).**

**MPHAMVU YA MWAZI WA YESU KWA ANTHU**

Satana amawopa kwambiri Mwazi wa Yesu, ndichifukwa chake safuna kuti magazi a Yesu agwiritsidwe ntchito chifukwa amanyamula Pangano la anthu ndipo ali ndi mphamvu zomugonjetsa makamaka m'masiku otsiriza ano.

**1.Mwazi wa Yesu** - umanyamula moyo, wathetsa imfa ndi kutipatsanso moyo. Mwazi wa Yesu watiyanjanitsa ndi Mulungu kudzera mu Pangano la Mwazi **Aroma 3:25.**

**2.Mwazi wa Yesu** - Watipanga kukhala chuma cha Mulungu, Mwazi uwu watigula ife m'manja mwa mdani ndi kutimasula. Tinagulidwa ndi Mwazi wamtengo wapatali ndipo tsopano ndife omasuka, **Chivumbulutso 5:9, Machitidwe a Atumwi 20:28, 1 Petro 1:18-19.**

**3.Mwazi wa Yesu –** unafafaniza machimo athu ndi kutipanga kukhala aufulu ndi atsopano, **Mateyu 26:27-28, Ahebri 9:22, 1 Yohane 1:7.**

**4.Mwazi wa Yesu -** Umatipatsa chitetezo padziko lapansi, umatiphimba ndi kutitchinjiriza ku mphamvu zamdima, matenda onse ndi zolimbana ndi mdani **(mdierekezi).**

**5.Mwazi wa Yesu -** Umatipatsa kulimba mtima kuti tipambane nkhondo yauzimu yomwe timalimbana nayo ndi mdierekezi ngakhale kutha kuyandikira mpando wachifumu wa Kumwamba chifukwa watiyeretsa ndi kutipatsa chisomo pamaso pa Mulungu, **Ahebri 10:19.**

## NYIMBO

*Mwazi wa Yesu × 3*
*Amatsuka kwathunthu,*
*Ndipo mphamvu za mdierekezi zagonjetsedwa ndi Yesu × 3*
*Matamando akhale kwa Mpulumutsi*
*Ndipo mphamvu za ziwanda zagonjetsedwa ndi Yesu × 3*
*Matamando akhale kwa Mpulumutsi.*
*Tsiku lina Yesu, adzabwera × 3 Kukatenga mpingo.*

## MPHAMVU YA MTANDA WA YESU KWA ANTHU

Muli mphamvu pa Mtanda, Kupyolera pa kupachikidwa kwa Yesu tamasulidwa. Mphamvu ya Mtanda yamasula miyoyo yathu ku imfa ndi imfa ndi kulandira moyo wosatha. Tikukhala ndi Yesu Khristu kudzera mu mphamvu ya mtanda tidalandira pa mtanda. Aliyense amene akhulupilira Yesu adapachika thupi lake ku imfa ndi kulandira moyo wosatha pamodzi ndi Yesu. Tinali akufa chifukwa cha uchimo ndipo tsopano tikukhala ndi Yesu.

1. **Mphamvu ya Mtanda** - yaombola miyoyo yathu. Moyo ndi munthu wanu wamkati amene amakhala kosatha amene amanyamula mzimu mwa iye amene Yesu anamugula pa mtanda ndi kumumasula ku chiweruzo cha Gahena ndi kulowa mu moyo wosatha **(Ufumu wa Kumwamba)** wa Mulungu wamoyo.
2. **Mphamvu ya mtanda** - yaombola miyoyo yathu ndi kutimasula.
3. **Mphamvu ya mtanda -** yatipatsa ife ulamuliro, kulamulira padziko lapansi ndi Yesu Khristu, **Luka 10:19**.
4. **Mphamvu ya mtanda -** Imatizindikiritsa ife mu dziko la uzimu kuti ndife a mu Ufumu wa Kumwamba. Tasindikizidwa pamphumi pathu kuti ndife a Ufumu wapamwamba, mdierekezi alibenso mphamvu pa ife, tamasulidwa.
5. **Mphamvu ya mtanda -** Yatipatsa ife chilolezo cha mkwatulo wa mpingo.

**6. Mphamvu ya Mtanda -** Yatipatsa kuwala, kudzera mwa Yesu takhala Kuwala chifukwa Khristu ndiye kuunika kwa dziko lapansi.

Tinagulidwa ndi mtengo waukulu pa mtanda ndi mwazi wa Yesu ndi mphamvu ya mtanda. Osadetsa mwinjiro wanu wachiyero umene munavala pamene munalandira Yesu monga Ambuye ndi Mpulumutsi wanu. Tsopano mwasanduka kachisi wa Mzimu Woyera, choncho khalani ndi moyo wachiyero tsopano. Musanayambe kupemphera, pempherani pemphero la kulapa kuti mukaima pamaso pa Mulungu mukhale oyera komanso kuti mapemphero anu akhale oyera pamaso pa Mulungu. Onse amene apulumutsidwa, akutetezedwa ndi mphamvu ya Mulungu, atazunguliridwa ndi moto woyaka **(moto wa Mzimu Woyera)**, ndipo Mwazi wa Yesu wawaphimba nthawi zonse, angelo oyera amawateteza. Pamene mudapulumutsidwa mudachoka m'dzikolo la ufumu wamdima ndi kulowa m'dziko la ufumu wa kuunika.

✞

## MAPEMPHERO OMASULA KU ZOMANGIKA ZOSIYANASIYANA NDI MATENDA

### KUWONONGA MAPANGANO A MDIMA M'MABANJA ATHU.

Abambo m'dzina la Yesu Khristu waku Nazareti wamoyo, ndikuphwanya ndikuwononga guwa lililonse lomangidwa kapena lolumikizidwa ndi ine kudziko la mizimu mdzina la Yesu.Ndimadzipatula ndekha, mzimu wanga, moyo wanga wonse ku guwa la mdima la banja langa. Ndimatumiza Angelo Oyera kuti agwire mizimu yonse yonyansa, kuimanga ndi kuiwotcha ndi moto wa Mzimu Woyera mdzina la Yesu.

Ndimagwiritsa ntchito Mwazi wa Yesu, kuletsa ndikuphwanya temberero lililonse ndi pangano lopangidwa ndi akulu abanja langa ndikundimanga. Kwalembedwa, **Chivumbulutso 12:11;**

*“Ndipo iwo anamlaka Iye ndi mwazi wa Mwanawankhosa, ndi mawu a umboni wawo; ndipo sanakonda moyo wawo kufikira imfa.*

Ndimagwiritsa ntchito Mwazi wa Yesu kuswa ndikuchotsa mapangano onse oyipa. Ndikuwotcha ndi moto wa Mzimu Woyera maguwa onse oipa. Ndimagwiritsa ntchito Lupanga lomwe ndi Mawu a Mulungu, kuti ndidule mgwirizano pakati pa ine ndi guwalo ndikudzimasula ndekha. Ndimagwiritsa ntchito Mwazi wa Yesu kufafaniza dzina langa m'buku la pangano loyipa la milungu ndikulemba dzina langa mu Bukhu la moyo wosatha. Ndikupanga Pangano latsopano tsopano ndi Mwazi wa Yesu pazipata zanga, chuma changa, mbadwa zanga ndi chilichonse chokhudza ine. Ndimalola Mwazi wa Yesu kuti ulankhule zabwino pa ine ndi chilichonse chomwe chikundikhudza tsopano ndi nthawi zonse. Zikomo Ambuye Yesu pondimasula ndikupanga pangano ndi ine kosatha ,**Amen.**

## MAPEMPHERO KWA KUCHIRITSIDWA KWA ODWALA

O Ambuye Yesu, ndikupemphani kuti mundikhululukire machimo onse omwe ndidachita modziwa kapena mosadziwa, potsegula zitseko zanga zauzimu ndikulola mdani kubzala chiwonongeko ndi matenda mwa ine. Ndikupempha kuti mufufute zolemba zanga zonse zaupandu zomwe zabwera pamaso panu ndi Mwazi Wanu **(Mwazi wa Yesu),Zalembedwa mu Yesaya 53:5;**

*“Koma iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu, ndi chilango chake ife tachiritsidwa.”*

M'dzina la Yesu Khristu waku Nazareti, ndikukana matenda ndi goli la mdani, ndaomboledwa ndi Mwazi wa Yesu. O matenda, ndikukana mdzina la Yesu, ndikulumbirira muulamuliro wa Dzina la Yesu, siya moyo wanga, choka ndipo usadzabwerenso. Ndimawononga maguwa onse oyipa, malinga, zopereka ndi matemberero omwe amanenedwa motsutsana ndi moyo wanga ndi thanzi langa ndi Mwazi wa Yesu.Ndiponya kugahena wansembe wa guwa la nsembe amene adandimanga mdzina la Yesu. Ndimafafaniza dzina langa, mthunzi wanga ndi chilichonse chogwidwa ndi mdani ndi Mwazi wa Yesu.M'dzina la Yesu ndikuthyola goli la mdani ndikuyika goli lopepuka ndi lofewa la Ambuye Yesu tsopano. Ndimalola Mwazi wa Yesu kuyeretsa thupi langa lonse ndikundimasula kwamuyaya. Ndikulengeza moyo pa ine tsopano ndi nthawi zonse, zikomo Ambuye Yesu chifukwa chondichiritsa ndikundimasula ,**Amen.**

## PEMPHERO LA M’MAMAWA KUDALITSA TSIKU LANU

Ambuye ndi mulungu wanga, amene muli kumwamba, ndikukuthokozani ponditeteza ine usiku onse ndi kundipatsa ine chisomo kuona tsiku latsopano. Atate, ndikuti zikomo pachikondi chanu pondipatsanso ine mphweya, ndi pondilora ine kukhala m’modzi mwa anthu amene akukhalabe ndi moyo m’dzikoli, Ndipereka tsiku langa lonse m’dzanja lanu, nditsogoleleni ndi ndikunditeteza pamene ndikupita kubwera ndi mwazi wanu, Ndatseka genena, imfa chionongeko ndi choipa china chilichonse chokonzedwa ndi m’daniyo kwa ine lero. Ine ndikulengeza kuti ilibe mphamvu pa ine mudzina la Yesu. msampha wina ulionse ndi chikonzero china chili chonse cha satana, chokonzedwera ine

ndi onse apabanja langa, ndikuziononga ndi kuzimwaza ndi mwazi wa Yesu. Tembelero ine iliyonse imene yatumizidwa ndi mawu ena zoipa oyankhulidwa motsutsana nane ndi mwazi wa Yesu. ndikulora Angelo oyera kunditeteza ine lero kuli konse ndipita pamene ndilowa ndi kutuluka mudzina la Yesu.Ndidalitsa za kudya zones ndi zakumwa zomwe ndidya lero ndi mwazi wa Yesu, ndikulengeza madalitso ndi chipambano change lero mudzina la Yesu. Ndikuthokozani ambuye Yesu ine kunditeteza ndi pondipatsa Angelo anu oyera kunditeteza lero, **Amen.**

**<u>PEMPHERO LA USIKU SADAGONE</u>**

Ambuye wanga ndi mulungu wanga, amene munakhala mwamba, mfumu ya mtendere ndi nulungu wa mphamva. Oyamba ndi otsiliza. Ndikuthokozani Kamba ku chitetezo chimene mwanditeteza ine tsiku lonse. Tate ndikuthokozani Kamba ka chikondi chanu, chitetezo pa ine kuchokera m'mamawa, masana ndi pano pamene ndikupita kukapumola usiku. Ndikupempha chikhululukiro chanu ndi chifundo ku machismo onse amene ndichita lero.

Ndikupemphani mufufute dzina langa mbuku la gehena ndi imfa ndi kulemba dzina langa m'buku la moyo wosatha.
Ndikuimitsa zonamiziridwira ine ndi mwazi wa Yesu ndi kuotcha kukhala phulutsa ndi moto wa mzimu oyera mu dzina la Yesu ndikugwetsa khoma lina lililonse loipa imene m'dani adakweza pa ine lero, mudzina la Yesu. Ine ndimila, mwana wanga ndi onse apelekedwa kwa ine mu mwazi wa Yesu usiku onse mu dzina la Yesu. Zikomo ambuye Yesu, ponditeteza ine,**Amen.**

## PEMPHERO LOBWEZELETSA CHIMENE CHIDABEDWA

Mudzina la Yesu Khristu, mwana wa Mulungu wa moyo. Ndikulamula zinthu zanga zonse zidabedwa ndi m'dani kundi bwezera ine mudzina la Yesu. Ndikuphwasula ndi kuononga nsembe ina iliyonse yopelekedwara ine ngati pangano loimitsa zinthu zanga, mu dzina la Yesu. Ndikugwilitsa ntchito mwazi wa Yesu kukhazika chete ndi kufufuta msembe yopelekedwa m'mawa oyankhula imfa, chiononongeko ndi choipa chotsutsana nane pa moyo wanga mu dzina la Yesu. Ndigonjesa mphamvu zonse zoipa mu dzina la Yesu. Ndasankha Yesu Khristu moyo wanga, pachifukwa chimenecho, Ndine omasulidwa ku mphamvu yoipa ya m'dima,Ndikutumiza Angelo ambuye ndikulondola zonse zimene zidabedwa kwa ine ndi kubwezeletsa kwa ine mudzina la Yesu. Ndikukana zinthu zanga kugwilitsidwa mu ufumu wa m'dima. Ndikulota kugwilitsidwa ntchito basi pachilinga cha ambuye ndi ufumu wake **(ufumu wakumwamba)** Zikomo ambuye Yesu ponditjjandiza ine ndi kundipatsanso chimene chidabedwa,**Amen.**

## UTHENGA WANGA KWA INU

Zabwino zonse posankha Yesu Khristu ndi kusankha madalitso. Yesu ndi njira yonkhayo ya mwamba munthu sadzapita kumwamba opanda Yesu Khristu mwa iye. Yesu Khristu ndi ulalo pakati pa ife ndi Mulungu wakumwamba. Khalani okonzeka kuyesero iliyonse imene mudutsemo, kukhala opatulika, nkhondo, kulakwilidwa, kuoneledwa pansi ndi zina zambiri. Musadere nazo nkhawa, pitilizani ndi chipulutso ndi kuzindikira kuti akuyesera kukuopyezani, inu

kuti musiye chipulumutso chanu ndikubwelelanso ku ndende ya satana. Pamene mwa pulumutsidwa mumalandila madalitso onse, zisomo ndi malonjezo onse amulungu ngati mwa wa mulungu, ndipo satana samazikonda zimenezo, ndi chifukwa chake nkhondo ndi chokubwezeletsa ku ndende ndi moyo wa ukapolo. zindikilani kuti kunzunzika kwanu sikwamuyaya, khulupililani mwa Yesu Khristu ndi mphamvu yake adzakupulumutsani ku nsampha wa m'dani chifukwa amakhala pa tsogolo pathu. welengani mawu amulungu **(BAIBULO)** satana, kudya pemphelani, chitani ntchito zabwino, imvani mawu amulungu amene muli chowona cha akapolo ake. ndikufunilani inu ochuluka ndi chipambano chachikulu mu ulendo wanu wachipulumutso kufikira Yesu adzabwelenso ndikutenga anthu ake, ndikudalitsa inu mu dzina la Yesu Khristu.

Perekani chopeleka chanu ku manambala awa;
**Dzina: Jesus Christ Ambassadors**
**M-Pesa: +255755734678**

Ambuye akudalitseni kwambiri, akuchulukiseni ndi Ambuye akukumbuleni chuma chanu kumwamba, **Ameni**

***Wolemba bukuli;***
***Petrida Karch***
***Imelo: petridakarch@gmail.com***
***+491758114293***